

KODI ANENERI
A
MULUNGU
ABRAHAMU,
MOSE,
YESU
NDI
MUHAMMAD

(MADALITSO NDI MTENDERE WA MULUNGU ZIKHALE PA IWO)

ANKAPEMBEZA BWANJI

?

kodi aneneri a Mulungu awa Abrahamu, Mose, Yesu ndi Muhammad (madalitso ndi mtendere wa mulungu zikhale pa iwo) ankapembeza bwanji?

Nthawi ina yake Sheikh Ahmed Deedat, amene ali womphunzira wachisilamu wankulu adayendera m'dzinda wa Jeddah womwe ukupezeka mu dziko la Saudi Arabia ndipo Sheikhwewa adatilongosolera ife zina mwa zinthu zomwe zidawachitikira pa umoyo wawo.

Iwo adati tsiku lina adatenga gulu la Akristu ndi Ayuda kuti akaone m'zikiti winawake mwa mizikiti ya mudzinda wa Durban m'dziko la South Africa. Ndipo panthawi yomwe adalowa mu m'zikiti Deedat sanangovula nsapato yekha ayi koma adaliwuzanso gulu lija kuti nalo livule nsapato ndipo gululo linamvera ndikuchita chimodzimidzi.

Ndipo zitachitika izi Deedat anafunsa gulu lija ngati linali kudziwa chifukwa chovulira nsapato mu m'zikiti. Gulu lija linayankha kuti "ayi, sitikudziwa". Pamene anayankha choncho, Deedat adalongosola kuti panthawi yomwe Mose adapita kuphiri la Sinai Mulungu analankhula kwayi:

Ndipo iye anati, usayandikire kuno; bvula nsapato zako kumapazi ako, pakuti pamalo pamene upondapo iwe, mpopatulika. (Eksodo3:5)

Atalongosola izi, munthawi yoti gulu lija linali chikhalire muzokhalira uku liri tcheru kuonera, Sheikh Ahmad Deedat analipempha gulu lija kuti limulole kuti akapange uzu (Ablution). Atamaliza uzu uja anabwerera kugulu lija ndikulifotokozerera kuti ndithu uzuwu sikuti uli pa malo apamwamba pokha kumbali ya ukhondo ayi- chifukwa asilamu amapanga uzuwu kasano patsiku-koma kuti chiyambi chakenso chimabwerera ku mbiri zakale zofunika. Apano mpamene anabweretsa mawu awa:

Ndipo Mose ndi Aaroni ndi ana ace amuna anasamba manja ao ndi mapazi ao m'menemo; 32 pakulowa iwo m'chihema chokomanako, ndi pakuyandikiza guwa la msembe anasamba; monga Yehova adamuza Mose. (Eksodo 40:31-32)

Pambuyo poti Sheikh Deedat apemphera swalat yokakamidwa (Faradhwi) anapitanso ku gulu lomwe anabwera nalo lija lomwe panthawiyi linali ndi chidwi kwambiri kuyang'ana asilamu ena mu m'zikitimu omwe amapemphera mapemphero ongozipereka (omwe amatchedwa kuti ma sunnah). Anayamba kulilongosolera gululi kakhalidwe kosiyanasiyana komwe amachita munthu amene akupemphera, maka kugwetsa nkhope pansu. Sheikh Deedat anasindikira mawu ake ponena kuti ndithu kugwetsa nkhope pansu ndikomwensho aneneri onse amachita pamapemphero awo. Adasindikanso mawuwa popereka maumboni nati:

Ndipo Abramu anagwa nkhope pansu, ndipo Yehova ananena naye kuti, ... (Genesis 17:3)

Ndipo Abrahamu adagwetsa nkhope pansu, ... (Genesis 17:17)

Ndipo Mose ndi Aaroni anachoka pamalo pa msonkhano kumka ku khomo la cihema cokomanako, nagwa nkhope zao pansi; ndipo ulemerero wa Yehova unaonekera iwo. (Numeri 20:6)

Yoswa anagwa nkhope yace pansi, napembedza,... (yoswa 5:14)

Ndipo anamuka patsogolo pang'ono, nagwa nkhope yace pansi, napemphera,... (Mateyu 26:39)

Ndipo kenaka Deedat analiwuza gulu lija kuti iwo (Akristu ndi Ayuda) amadziwa bwinobwino njira ya kapembezidwe yomwe iwo amatsata ndikofunika kuti tsopano adzindikire kapembezidwe ka asilamu.

Mwa ubwino ndimoleza mtima, Deedat adalifunsa gulu lija kuti ndi njira yiti yakapembezidwe yomwe ili yoyandikira kwambiri kwa yesu?

Wonse Akristu ndi Ayuda mogwirizana anayankha kuti ndithu njira yakapembezidwe ka Asilamu ndiyomwe ili yoyandikira kwa Yesu kuposa ena onse.



Akristu ambiri omwe akumabwerera kuchisilamu akumayikira umboni kuti pamene iwo ali asilamu ndipomwe ali akristu abwino kuposa mmene analiri kale. Potengera kuti liwu loti “Mkristu” limatanthauza kuti “otsatira a“Yesu”.

Nanga ndichifukwa ninji anthu awa omwe tsopano ndi asilamu akumadzitcha kuti iwo ndi amene ali chifupi potsatira Yesu?

Tatiyeni tiganizire mozama bwino pamenepa. Chifukwa titati tiyang’ane bwino mmene Chipangano Chakale chikunenera pankhani yokhudza Yesu (A.S)tikupeza malo ambiri onena kuti yesu anali kuyika nkhope yake pansi popemphera analinso kulonjera otsatira ake pogwiritsa ntchito mawu amtendere komanso anali akusala kudya nthawi yayitali.

Ndithudi akristu oyambirira anali akudzindikira bwino lomwe kuti iwowo anali asilamu- ndi tanthauzo lonse la liwuli- asanazitulukire zinthu zovomereza ndi kulimbikitsa zikhulupiriro zawo zachibadwidwe kudzera mu malemba a Qur’an yolemekezeka yomwe Mulungu anayibvumbulutsa kwa mneneri omaliza Muhammad (S.A.W).

E,inu amene mwakhulupirira! Weramani ndikugwetsa nkhope zanu pansi Ndipo mpembezeni Mbuye wanu ndikuchita zabwino kuti mupambane. (Qur’an 22:77)

Kodi simukutha kuona kuti kukonzeka ndi kuvomereza za umodzi wa Mulungu sizilekana ndi chibadwidwe chamunthu?

Koma lero anthu amene amati akutsatira njira ya Yesu, Abrahamu,ndi Mose(A.S)atsemphana ndikutalikana kwambiri ndi njira yowongoka imeneyi.

Ndipo tikati tikambe zachi Kristu, tipeza kuti anthu achisintha chikhulupiriro chonse mwabodza pankhani yokhudza bwana wathu Yesu (A.S), ndipo zotsatira zake ndikumuyika iye kukhala chinachake chomwe iye mwiniwache sanazitchepo ngakhale ndi tsiku limodzi.

Tsopano zifunsemi nokha moopa Mulungu, ndindani lerolino amene akutsata chitsanzo cha Yesu molungama? Monga mukudziwa, ndithu asilamu amapemphera modzipereka uku akugwetsa nkhope zawo pansi kasanu patsiku.

Ndithu asilamu akutsatira chipembezo cha Yesu (A.S); mosapeneka ndiye kuti akutsatira chikhulupiriro chomwe Yesu anachikamba komanso kuchichita. Chimodzimodzinso, asilamu amapembeza Mulungu yemwe Yesu (A.S) anali kumpembeza; Mulungunso wa Abrahamu, Mose ndi Muhammad (S.A.W). Kuonjezera apo, asilamu nthawi zonse amapatsana malonje amtendere ponena kuti” mtendere ukhale kwainu” ndipo malingana ndi mmene Yesu (A.S) adasalira kudya masiku makumi anayi muchipululu, asilamu amasala kudya mwezi onse wa Ramadhan.

Pomalizira, tiyeni tonse tipemphere mozichepetsa monga mmene amapempherera aneneri onse a Mulungu. Ndikukuitanirani ku website yathu kuti muthe kupanga download buku lophunzitsa ndondomeko ya salat.